Dongosolo la Mpingo

Ife tangotseka kumene msonkhano waukulu, wa mausiku asanu ku kachisi, komwe, mwa chisomo cha Mulungu ndi mwa kuthandiza Kwake, ine ndayesera molimba, mwa Lemba, kuti ndiyike mu dongosolo Mpingo wa Ambuye Yesu Khristu, momwe ife timakhulupirira pa Branham Tabernacle.

2 Chinthu choyamba chimene ine ndikukhumba kuti ndinene ndi chakuti m'busa ali nthawizonse mu ulamuliro wathunthu wa pa kachisi, mu kusakhalapo kwanga, ndipo ine ndimangoyang'ana kwa abusa pamene ine ndibwerera. Kotero, iye ali mu ulamuliro wathunthu kuti asinthe kapena kuti achite chirichonse chimene iye akuganiza kuti ndi chopambana pansi pa ulamuliro wa Mzimu Woyera, pamene ine ndiri kwina.

3 Ife timakhulupirira mu Mpingo wautumwi, kuphunzitsa Dalitso lautumwi kwa anthu a tsiku lino. Ife timakhulupirira mu Uthenga wamphumphu, ndipo timakhulupirira kuti zizindikiro zonse ndi zodabwitsa zimene zinayankhulidwa, ndi Ambuye wathu Yesu Khristu, zikanamatsatira Mpingo Wake mpaka Iye atabweranso. Ife timakhulupirira mu zinthu zimenezo, ndipo timakhulupirira kuti izo ndi zoti ziziyikidwa mu dongosolo, kuti Mpingo uli ndi dongosolo Lake. Ndipo mpingo uliwonse uli ndi chiphunzitso chake, ndi dongosolo, ndi khalidwe.

4 Mpingo wathu ulibe mamembala ngati ojowina. Ife timakhulupirira kuti Mpingo wonse wakonsekonse wa Mulungu wamoyo, uli abale athu ndi alongo; ndi kuti anthu onse ali nthawizonse olandiridwa, mosalabadira chipembedzo chimene iwo ali a icho, ku Branham Tabernacle, pa 8th ndi Penn Street mu Jeffersonville, Indiana.

5 Ife timakhulupirira mu "kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro," Aroma 5:1. Ife timakhulupirira kuti, munthu atalungamitsidwa mwa chikhulupiriro, iye amakhala nao mtendere ndi Ambuye Yesu Khristu. Koma ndi zotheka kuti munthu yemweyu akhoza kukhala ndi zizolowezi monga ngati, kumwa, kusuta, kuchita zinthu zomwe iye sayenera kumachita, zizolowezi zauve za thupi.

6 Ndiye ife timakhulupirira kuti Magazi a Yesu Khristu amamutsuka munthu uyu kuti awatumikire Ambuye. Ndipo ndizo, ife timakhulupirira mu "kuyeretsedwa" molingana ndi Ahebri 13:12 ndi 13, "Pamene Yesu naponso, kuti Iye akawayeretse anthu ndi Mwazi Wake Womwe, anamva kuwawa kunja kwa chipata." Ndipo ife timakhulupirira kuti kuyeretsedwa kumaphunzitsidwa mu Chipangano Chatsopano, ndipo ndi za kwa okhulupirira kudutsa mu m'badwo wa Chipangano Chatsopano, umene ife tiri kukhalamo

tsopano. Ndipo ife timakhulupiriranso kuti munthu akakhala atayeretsedwa kale, makhalidwe oyipa achoka kwa munthuyo.

7 Iye ndi wokhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu, ndipo zizolowezi zake zapita, ife timakhulupilira kuti ndiyeno iye ndi woyenera "ubatizo wa Mzimu Woyera," omwe umabwera ngati chomudzaza cha wokhulupirirayo. Ndiyeno pamene wokhulupirira . . .

8 Ziri basi, nthawi zochuluka zimene ine ndaphunzitsa izi, monga kutola galasi mu khola la nkhuku. Kulungamitsidwa, ndi kulitola ilo, kukonzekera kuti muziligwiritsa ilo ntchito, muli ndi cholinga mu mtima. Ndi zimene Mulungu amachita kwa wochimwa. Iye akadali wauve.

9 Ndiye iye amayeretsedwa ndi Magazi a Yesu Khristu. Ndipo mawu oti kuyeretsa ali mawu apawiri, amene amatanthauza, "kuyeretsedwa, ndi kuyikidwa pambali kuti chitumikire." Mu Chipangano Chakale, guwa linkachiyeretsa chipangizo, ndipo icho chinkaikidwa pambali kuti chitumikire ntchito.

10 Ife timakhulupilira kuti Mzimu Woyera uli kuyika chipangizo chomwecho mu kutumikira. Kuti, Mzimu Woyera si uli sitepe ina ya chisomo, koma kuchulukira kwa chisomo chomwecho, chimene chimamudzaza wokhulupirira mpaka pa muyezo wakuti zizindikiro ndi zodabwitsa, monga ngati mphatso zautumwi zoyankhulidwa mu Akorinto Woyamba 12, zimadziwonetsera zokha kudzera mwa wokhulupirira uyu, pamene Mzimu Woyera ubwera umo kudzatengapo mphatsozo.

11 Ine ndikukhulupirira kuti Malemba amatiphunzitsa kuti "mphatso ndi maitanidwe ziri zopanda kulapa," kuti pamene ife timabadwa mu dziko lino, ife timatumizidwa kuno mwa cholinga chimodzi, chimene chiri, cha Mulungu. Ndipo kuti ife tisanakhale ngakhale okula, pamene ife tikadali ana, mphatso zomwe ife tinali nazo kuchokera kwa Mulungu zimakhala ziri mkati mwa ife apo, ndipo kudzaza kokha kwa Mzimu Woyera kumaika mphatso zimenezi mu kugwira ntchito; koma ife timakhala tiri nazo izo pachiyambi, monga ngati aphunzitsi, ndi atumwi, n—ndi aneneri, ndi mphatso za malirime, ndi mphatso zisanu ndi zinai zauzimu molingana ndi Akorinto Woyamba 12. Tsopano, ife tikukhulupirira kuti mphatso zimenezi ziri nkugwira ntchito lero, ndipo izo ziyenera kuti zizikhala mu mpingo wamba uliwonse.

12 Ngakhale, potero, ife tapeza, kudutsa mu dziko lonse, kuti pali kutengeka kochuluka kumene kwakakamira pa anthu amene akudzinenera kuti ali okhulupirira mwautumwi. Monga momwe iwo aliri mu madongosolo enawo, ndi mwina motero, ife tiri nawo otengeka. Izo zakhala kwina konseko, ife takhala tiri nazo izo kudutsa mu mibadwo. Iwo anali nazo izo mu masiku autumwi; ndipo monga Paulo ananena pamenepo, kuti momwe ena anadzera ndipo "anawakakamizira

iwo kuti achoke, natsatira ziphunzitso zina," ndi zina zotero. Koma mu Kuphunzitsa kwake komwe, iye anati, "Ngati Mngelo wochokera Kumwamba ati adzaphunzitse china chirichonse," kuposa zimene iye ankaphunzitsa, "msiyeni iye akhale wotembereredwa."

13 Kotero, ife, ngati Branham Tabernacle, pa 8th ndi Penn Street pano, tikuyesera kuti tizitsatira Ziphunzitso za Chipangano Chatsopano. Pakuti, ife tikukhulupirira Kuti, "Yesu Khristu, pokhala Mwana wa Mulungu." Ndi Paulo mtumwi anali chotengera choitanidwa ndi chosankhidwa, mwa kusankha kwa Mulungu, kuti atumizidwe kwa Mpingo wa Amitundu, kuti akawuike iwo mu dongosolo.

14 Tsopano, ife timakhulupirira mu "ubatizo wa madzi," mu Branham Tabernacle, mwa kumiza, "mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu," chimene chiri Chiphunzitso chautumwi cha Baibulo. Ndipo zikhale kuti mamembala onse a ife, kapena obwera ku Branham Tabernacle, amene akukhumba izo, pa nthawi iliyonse, (kupempha kuti) amizidwe, mu Dzina la Ambuye Yesu. Iye aziwafunsa abusa; ngati iwo alapa, ndi kukhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu, abusa atero, mwamsanga momwe zingathekere, ngakhale pomwepo ngati iye angathe, kuwabatiza iwo mwamsanga. Izi zimawabweretsa iwo mu chiyanjano cha okhulupirira. Ife tikukhulupirira kuti mwa ubatizo wa madzi ife timabweretsedwa mu chiyanjano.

15 Koma, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera, ife timabweretsedwa mu mamembala, kukhala mamembala a Thupi la Yesu Khristu, lomwe liri konsekonse mdziko.

16 Tsopano chinthu china chimene ife timakhulupirira, nkuti, "Mawonetseredwe a Mzimu amaperekedwa kwa munthu aliyense kuti azipindule nawo." Tsopano, ife timakhulupirira kuti pamene mphatso izi, ndi zina zotero, ziri kugwira ntchito mu Mpingo; chimene, ife timachifuna ndipo timachikhumba kuti anthu amene ali amphatso, mwa Mzimu, azibwera ndi kumadzapembedza nafe.

17 Tsopano, mu malo ochuluka, ife timapeza kuti pamene mphatso izi ziri mwa anthu, anthuwo samamvetsa motani ndi liti kuti azigwiritsa ntchito izi, ndipo, pakuchita choncho, iwo amangobweretsa chitonzo; chimene ife tikukhulupirira kuti zingakhale basi chimene Satana angachite kuti awapangitse akunja, osakhulupirira, ndi ena otero, kumawopa Dalitso lodabwitsa ili limene Mulungu walipereka kwa Mpingo mu masiku ano.

18 Paulo anati, "Pamene abwera mlendo pakati pathu, ndipo ife tonse nkumayankhula ndi malirime, kodi munthuyo sapita kwina nkumakanena kuti ife 'tapenga'? Koma ngati wina angalosere, ndi kupangitsa kudziwika chinsinsi cha mu mtima,

ndiye iwo angagwe pansi ndi kuti, 'Zoonadi, Mulungu ali ndi inu.'"

19 Tsopano, ife tikukhulupirira kuti mphatso zauzimu, pakati pa okhulupirira, ndilo dongosolo la tsikuli. Ife sitingathe kukhulupirira kuti munthu angathe kumalalikira pansi pa Kudzodza ndipo (kenako) nkukhala mphunzitsi wodzozedwa, ndiyeno nkumakana mphatso ya machiritso, kapena mphatso ya ulosi, kapena kuyankhula ndi malirime, kapena kutanthauzira kwa malirime, kapena iliyonse ya mphatso zina izi.

20 Kotero, choncho, aka ndiko kakhulupiriridwe kanga mu Mawu a Mulungu, momwe Branham Tabernacle, pa 8th ndi Penn Street muno mu Jeffersonville, ikuyenera kumayendetseredwa. Ine ndikuganiza, chinthu choyamba, ndipo ndikukhulupirira kuti zinthu izi zimene ine ndikuzinena ziri zofunikira ndipo ziyenera kuti zizichitidwa mwa njira iyi, mu Branham Tabernacle, kuti iwo uzichita bwino mwa Ambuye. Ndipo ngati pa nthawi iliyonse izi, Ichi, chingati chifunsidwe, munthu amene amene ali mu funso pa Zimenezi akhoza kundifunsa ine ngati iwo sangathe kufika kwa abusa, kapena iwo angathe kuwafunsa abusa. Ngati ine ndiri kunyumba, nditachokapo mu ena a maulendo, ine ndidzakhala wokondwa k—kumuthandiza ngakhale membala kapena m'busa, pa nthawi iliyonse. Ndipo zinthu izi ziri Mwamalemba, ndipo ine ndikukhulupirira kuti ilo ndi dongosolo la Mpingo.

21 Ine ndikuganiza, poyamba, kuti membala aliyense, kapena wopembedza aliyense, wa pa Branham Tabernacle, ayenera azikhala mochuluka kwambiri mu chikondi Chaumulungu kwa wina mzake mpakana (izo zingapangitse) mitima yawo ingamakhale ikufuna kuonana wina ndi mzake pamene iwo ali oti apite kutali, kusiyana wina ndi mzake pa utumiki, usiku. Ine ndine wokhulupirira moona mu "chikondi Chaumulungu." Mtumwi Paulo anati chimenecho chinali umboni wa Mzimu Woyera. "Mwa khalidwe ili, anthu onse adzadziwa kuti inu ndinu ophunzira Anga," anatero Yesu, "pamene inu muli nacho chikondi wina kwa mzake."

Ndipo ife tikukhulupirira kuti ndi chikondi cha Mulungu chimene chinamutumiza Yesu Khristu ku dziko lapansi, kuti adzatifere ife tonse. "Mulungu analikonda dziko kwambiri, Iye anapereka Mwana Wake wobalidwa yekha, kuti aliyense amene akhulupirira mwa Iye asati azitayika, koma akhale nawo Moyo wosatha." Ndipo Moyo wosatha apa uli "Moyo Wake Womwe wa Mulungu," chifukwa ife timakhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera; umene uli Mbewu ya Abrahamu, ndipo umatipatsa ife chikhulupiriro chimene Abrahamu anali nacho, pamene iye anamkhulupirira Mulungu iye asanadulidwe nkomwe.

22 Tsopano, chinthu chotsatira, ife timakhulupirira kuti opembedza awa ayenera "kumakomana palimodzi, anthu amphatso awa," monga ngati malirime, ndi anthu amene amapeza mavumbulutso ndi kutanthauzira, ndi zina zotero. Mamembala amenewa, kapena okhulupirira awa, kani, azibwera palimodzi mosachepera maminiti forte faifi kapena ora utumiki usanayambike konse. Tchalitchi chizikhala chitatsegulidwa molawirira, ndipo okhulupirira azibwera palimodzi pa mausiku amenewa, ndipo mosachepera maminiti forte-faifi mpaka ora utumiki usanayambe.

23 Ine ndikukhulupirira, pa Branham Tabernacle nthawizonse ayenera azikhala naye woimba limba wodzazidwa ndi Mzimu, amene angamabwere molawirira, atadzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo angamaimbe mofewa, mofewa kwambiri, nyimbo zauzimu, monga ngati, "Pamtanda paja pamene Mpulumutsi anafera, pansi apo pa kunditsuka ku tchimo ine ndinalira; apo kwa mtima wanga Magazi anagwiritsidwa ntchito, ulemerero kwa Dina Lake!" Chinachake pa dongosolo limenelo, "Pafupi, Mulungu Wanga, Kwa Inu." "Thanthwe La Mibadwo, long'ambidwira kwa Ine." Kapena, "Pafupi ndi Mtanda," kapena chinachake pa dongosolo limenelo; mofewa, mosafulumira, pamene iye akusinkhasinkha mowirikiza pa Mzimu Woyera, mwamuna kapena mkazi, aliyense amene angakhale ali.

24 Ndiye ine ndikukhulupirira kuti opembedza, akamalowa umo, azikhala akukomanidwa, ndipo apo azipachika zikhoto zawo ndi zipewa, kulozeredwa poti akakhale, ndi ulemu umene othandizira ndi madikoni odzazidwa ndi Mzimu Woyera angathe kuuchita, ndi mwa chikondi, kuti awone Mpingo wa Mulungu wamoyo ukupita patsogolo.

25 Opembedza awa asamayankhulane wina kwa mzake, ndi kumanena kwa wina, ndi kumapanga phokoso mu tchalitchi.

26 Iwo azibwera palimodzi. Poyamba, alowe mu pemphero la kachetechete, mwinamwake pa guwa, kwa mphindi zochepa. Popanda kupemphera komveka, inu mumusokoneza wina wakenso; pemphero lakachetechete, inu muli mu kupembedza. Kulola zimenezo zilowerere mkati. Kupembedza, mu mzimu wanu, kenako nkubwerera ku mpando wanu.

27 Kapena, inu simusowa kuti mupite ku guwa. Kungolowa umo ndi kukapeza pokhala panu, kukhala pansi, kumamvetsera kwa zing'wenyeng'wenye; kutseka maso anu, kuweramitsa mutu wanu; ndi, kukakhala mwa chete, kumampembedza Mulungu, utali wonsewo.

28 Ndiye ngati Mzimu uti uwulule chinachake kwa wina, k— kapena winawake kukhala atadzazidwa ndi Mzimu mpaka pa malo pamene iwo angayankhule ndi malirime, ndiye munthu uyu aziimilira ndi kupereka uthengawo. Ndipo aliyense ayenera kuti azigwira bata lawo mpaka kutanthauzira kutabwera.

29 Pamene kutanthauzira kwabwera, iko kusamakhale kuli basi kubwereza Lemba, kapena chinachake chimene chiribe tanthauzo. Iwo uyenera uzikhala uthenga wolunjikidwa kwa Mpingo, kapena ife tiganiza kuti izo zingakhale kuti zinali mwa thupi; ife timawona zochuluka kwambiri za izo. Ndipo tsopano, pamene ine ndikukhulupirira, m—Mzimu ukanati uyankhule kokha "pa kumangiriza kwa Mpingo."

30 Ndipo tsopano, uwo ukhoza kukhala uli uthenga, chinachake mwa dongosolo ili, mwinamwake. Mwinamwake athu akusonkhana pa nthawi iyi, anthu ena odwala abwera umo. Mwinamwake umo muli munthu wagona, wolumala kapena chinachake. Inu simunayambe mwamuwonapo iye kale. Koma pamene kutanthauzira kungabwere, iko kungakhale chinachake mwa dongosolo ili; pamene kutanthauzira, kapena wina amene wangoyankhulayo, angati anene, "Chabwino, PAKUTI ATERO AMBUYE, bambo amene ali pakati pathu wachokera ku malo akuti-akuti," ndi kuwalongosola malowo. Ndipo angati anene kuti, "Iye analumala chifukwa, zaka zitatu kapena zinai zapitazo," zirizonse zimene zingakhale, nkhaniyo ingakhoze kukhala ili, "iye anachita chinachake choipa," monga, "anamsiya mkazi wake ndi ana, ndipo anawathawira kwina kuwasiya iwo. Ndipo iye anagwa pa galimoto," kapena chinachake chonga dongosolo limenelo, "ndipo anavulala, ndipo zinamulumalitsa iye. PAKUTI ATERO AMBUYE. Ngati iye angalape za zimenezo, ndipo angalonjeze kuti abwerera kwa mkazi wake ndi kukadziyanjanitsa iyeyekha kwa iye, ndiye iye achiritsidwa tsopano ndipo abwerera kwa banja lake."

31 Ndiyeno wina aliyense asananene kanthu kena, apo payenera kukhala pali mosachepera awiri, kapena opitirira, amuna kapena anthu mu chipindacho, amene ali mwauzimu olimba mu Chiphunzitso cha Uthenga, amene ali nako kuzindikira kwabwino kwa mzimu, kuti aimilire apo ndi kuti "Izi ndi za Ambuye."

32 Ndipo ngati chinthu ichi sichichitika, ndiye malirime asati azitchulidwa mu mpingomu. Ngati munthu ayankhula ndi malirime, Paulo anati, "Ngati apo palibe wotanthauzira," ndi zina zotero, "asiyeni iwo azikayankhulira kwawo," kapena kulikonse kumene kungakhale kuli, "pakuti iwo akungodzidalitsa okha, ndipo si za kumangiriza kwa Mpingo."

33 Ndipo munthu uyu, atatha kuyankhula, ndi kutanthauzira; ndiyeno oweruza awiri kapena atatu, molingana ndi Chiphunzitso cha Paulo Woyera cha Baibulo, kuti izo ziyenera kuti "ziziweruzidwa ndi oweruza awiri kapena atatu."

34 Ndiye zimulolani munthu amene Iwo ukumutchulayo, kuti apite. Ndipo mwinamwake Iwo ungati uzipereke izo kwa munthu winawake, kapena m'busa kapena winawake, kuti apite akayike manja pa munthu ameneyo, ndipo iye amene

akudwalayo kapena kusautsidwa, ndipo iwo achiritsidwa. Ndiye muloleni m'busa kapena munthu winayo, aliyense amene angakhale ali amene zinaperekedwa mwa Mzimu Woyera kuti apite "akapemphere pemphero la chikhulupiriro," aloleni iwo apite ndi kukatumikira kwa munthuyo molingana ndi zomwe Mzimu wanena. Ndiye pa nthawi imeneyo, munthu pa yemwe. . . Ndipo zirizonse zimene Mzimu Woyera unanena, izo zichitika, mosachedwa ndiye, monga momwe Mzimu Woyera waziperekera izo.

35 Ndiyeno anthu angathe kusangalala, ndi kukhala othokoza kwambiri, ndi kuyamika ndi kumupembedza Mulungu, chifukwa Mulungu amafuna kuti azipembedzedwa.

36 Ndiye iwo ayenera—ndiye iwo ayenera kuweramitsa mitu yawo ndi kukhala mu pemphero kachiwiri, kuti awone ngati apo pangakhale uthenga wina umene Mzimu Woyera ungafune kuti mphatso izi ziwonetsere, tisanati.

37 Ndiyeno ngati nthawi iliyonse imene munthu angayankhule mu malirime, ndi kutanthauzira, ndipo—oweruza angamutumize munthuyo kuti akatenge, kuti akachite chirichonse chimene chinanenedwa kuti chikachitidwe, ndipo icho sichiri kufika pochitika, ndiye gulu lonse la iwo lizipita ku guwa ndipo pamenepo nkupemphera kwa Mulungu kuti awutengere mzimu umenewo kutali ndi iwo, chifukwa palibe aliyense amene angamaufune Mzimu wonga umenewo. Ife tingadziwe kuti izo zikanakhala ziri zabodza, ndipo ungakhale uli wa mdani, ndipo osati wa Mulungu, chifukwa Mulungu anganene choonadi chokha. Lolani zimenezo zimveke bwino bwino kwa mpingo, inu musanayambe ili, dongosolo la tsopano ili.

38 Ndiye, kapena, mwinamwake izo zikhoza kukhala chinachake chonga ichi, uthenga unganene kwa m'bale winawake, mwinamwake kunena, kuti, "Amakhala mphepete mwa msewu wa njanji," kapena chinachake, "kuti akamupangitse iye kusamukapo, chifukwa padzakhala pali ngozi pa msewuwo," kapena chinachake, kapena chirichonse mu dongosolo limenelo.

39 Ndi kuwalola oweruza, atatha kuwupatsa mpingo chilolezo choti uyankhule, kapena kuti achite nawo uthenga uwu umene wangopitapo kumene, ngati kuweruza kwawo kuli, "Izo ndi za Mulungu," ndiye yang'anirani ndi kuona ngati izo ziti zifike pochitika.

40 Ndipo ngati izo zifika pochitika, muthokozeni Mulungu, ndi kukhala achisomo kwambiri, odzaza chisomo mu mtima wanu kwa Iye. Ndi kumupatsa Iye matamando ndi kumpembedza, ndi kukhala odzichepetsa. Pamwamba pa zinthu zonse, khalani odzichepetsa.

41 Musati konse mudzadzifikitse nokha podzitukumula mpaka pa malo pamene inu mukudziwa mochuluka kuposa abusa anu

kapena mpingo umene inu mukupembedzamo uwo. Ngati inu mufika pa malo amenewo, ndiye ine ndingakulangizeni aliyense wa inu kuti mukapeze malo ena oti muzikapembedza uko. Chifukwa, ine ndikuwapempha abusa kuti asadzaloleze konse chirichonse cha kunja kwa dongosolo la Baibulo, momwe ife taziwonera izo muno mu mpingo. Ndiyeno ife tikufuna mphatso zimenezi kuti zizigwiritsidwa ntchito, ndi mu malo ake, ndi opembedza. Ngati izo zikuchititsidwa molondola, mogwirizana ndi Mawu, inu muwona mpingo wamphamvu, wodabwitsa uli kugwirira ntchito kwa Ambuye wathu Yesu Khristu.

42 Tsopano, ndiye chinthu chotsatira chiti chizichitika, chikhala chiri choti ngati anthu awa amene ali, amene amachoka mu dongosolo mu nthawi imeneyi, kuti dikoni kapena wothandizira wina amene ali wodzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo ali ndi chisomo chochuluka mu mtima mwawo, azipita kwa munthuyo, mwaulemu, monga bambo, ndipo azikawakonza iwo mwa mchitidwe uwu. Kapena, m'busa, aliyense amene angakhale ali, zimene zingakhale zofunikira kwambiri kuti adikoni azichita choncho; pakuti abusa, pa nthawi imeneyi, pamene mautumiki auzimu awa ali kupitirira, ayenera kumakhala ali mu chipinda chopempherera, kapena kwinakwake, akupemphera.

43 Mauthenga awa, ndiye, ngati palibe mauthenga amene akuchitika, palibe mavumbulutso, ndiye anthuwo angakhale nawo mwayi, ngati iwo atafuna, kuti aziimirira ndi kupereka umboni, umboni wa ulemerero kwa Mulungu yekha. Iwo Sali okakamizidwira kuti achite izi, koma maumboni ayenera kuti aziperekedwa uthenga usanaperekedwe kapena utumiki uliwonse wa nyimbo usanayambe, kapena chirichonse, maumboni mu mautumiki a kupembedza awa.

44 Kodi inu mukumvetsa, mpingo, kuti, pochita izi, inu muli nawo mpingo wonse mu mzimu wa kupembedza, Mawu asanafike umo kuti aphunzitsidwe? Ndiye Mzimu Woyera uzilowa mu Mawu, ndi kuwonetsera Mulungu kudzera mu Mawu, chikhala chiri chitsimikiziro cha kupembedza kwanu.

45 Tsopano, ndiye zikatha izi, ndi nthawi ya abusa kuti abwere apo. Ngati mauthenga akupitirira, titi...Abusa azituluka ndendende, titi, hafu pasiti seveni, ndipo, kapena kotala ya eyiti. Ndipo ngati mauthenga awa ali kupitirirabe, abusa asanabwere kwawo...kuchokera kowerengera kwawo, kapena kulikonse kumene iwo angakhale ali, kuti adzatenge malo awo pa nsanja; m'bale wina azimulangiza iye, chifukwa oyera amadziwa kuti pamene abusa abwera pa nsanja, ndi nthawi yawo ndiye ya utumiki. Ndipo izo zimapereka nthawi yochuluka, yokwanira kwa kuwonetseredwa konse kwa mphatso, kuti zibweretse Mzimu wa Mulungu mu—osonkhana.

46 Ndipo ngati wosakhulupirira aliyense angapezeke ali pamenepo, nakhala mopanda dongosolo; munthu wamtima wachifundo angapite kwa iwo, monga ngati wothandizira kapena dikoni, ndipo angawauze iwo kuti iwo akanati—iwo akanati . . . apemphedwe kuti akhale molemekeza, kapena akhale olemekeza pamene utumiki uli mu dongosolo. Chifukwa, Mzimu uli mu nyumbayo, ndipo mphatso za Mulungu ziri kuwonetseredwa mwa kumangiriza kwa Mpingo. Ndipo munthu uyu aziwuzidwa mwa chikondi, ndipo osati mwaukali. Kupatula izo zitafika pa malo oti iwo anali kumwa, kapena kusamvera kwina, kapena chinachake chimene chingakhale chiri chosokonezana ndi kupembedza k—kwa Ambuye, pamene mphatso ziri nkuwonetseredwa; ndiye munthuyo ayenera, angakhoze, kapena azitulutsidwira panja ku mbali imodzi, ku chimodzi cha zipinda zakumbuyo, kapena kwinakwake, ndi kukayankhulidwa, ndi kuchita naye, mwachifundo.

47 Tsopano, abusa akanali akubwera ku nsanja. Pamene abusa abwera pa nsanja, ine ndingati, pa Branham Tabernacle pano, kuti abusa azitsogolera osonkhana mosachepera nyimbo imodzi kapena ziwiri zabwino. Pakuti ife tazipeza izo chomwecho, kuti pamene ochuluka kwambiri akuyesera kuti azichitapo mu mpingo, izo zimabweretsa apo vuto lokha. Ine ndingapereke lingaliro, momwe ine ndinkachitira pamene ine ndinali kuchita ubusa pa mpingopa; ine ndinkatsogolera nyimbo, mwiniwanga. Ndipo ine ndikumverera kuti icho chingati chikhale chinthu chabwino ngati abusa atamachita choncho, iwo okha.

48 Ndipo mu misonkhano yonse ya mapemphero, kumene iwo asonkhana palimodzi, gulu, msonkhano wa mapemphero, m'busa ayenera azikhala ali pa uliwonsewo. Izo asamazisiyire kwa munthu wina aliyense kuti azipita ndi kukatsogolera misonkhano yoteroyo. Pakuti ife tapeza chotero kuti iwo amachoka pa njirayo, pa chiphunzitso, ndiyeno iwo amayambitsa, iwo amazibweretsa izo mu mpingo momwe, ndipo, nthawi zambiri, zimabweretsa mipatuko, ndi zina zotero, zomwe si ziri za mu Mpingo wa Mulungu wamoyo. Ndipo abusa ayenera kuti azikhalapo pa misonkhano yonse ya mapemphero, ndi zina zotero, kumene kuso- . . . kusonkhana kuli.

49 Ndipo abusa asamatenge konse mbali mu msonkhano, pa kunena kuti pali gulu limodzi lomwe liri motere ndi lina liri motero. Mbusa akuyenera kuti aziima pakati pa onse awo, ndi kumapita kwa iwo, ndi kuwafikitsa iwo poyanjanitsidwa, mosachedwa. Ndipo ngati iye sangathe kuwayanjanitsa iwo, iye atenge dikoni limodzi naye. Ndiyeno ngati iwo samumvera ngakhale m'busayo kapena dikoni, ndiye izo ziziuzidwa kwa mpingo, ndipo, monga Yesu ananena, "Asiyeni iwo akhale kwa inu ngati achikunja ndi amisonkho." "Ndipo chirichonse chimene inu muchimanga padziko lapansi," Yesu anati, "Ine

ndichimanga Kumwamba, ndipo chimene inu muchimasula pa dziko lapansi, Ine ndizichimasula Kumwamba."

50 Tsopano, pamene abusa abwera pa nsanja, muziwalola abusawo ndiye kutsogolera, mosachepera, nyimbo imodzi kapena ziwiri, ndi kupita molunjika ku Mawu.

51 Palibe ayi nthawi ya misonkhano ya maumboni aatali awa, ndi aliyense kuwuka apo, ndi kukhala ndi mawu oti anenepo. Zimenezo sizimachita bwino mu Branham Tabernacle.

52 Ngati anthu aliwonse, amene akumvetsera kwa tepi iyi, ndipo, inu, ndipo izo zachitapo bwino mu mpingo wanu, chabwino, izo ziri bwino bwino mwangwiro. Ndipo ife tiri okondwa kwambiri pa izo, kuti izo zikuchita bwino mu mpingo wanu.

53 Koma mu chathuchi kuno, izo siziri kutero, izo zimangoyambitsa chisokonezo. Ine ndakhala ndikuchita ubusa pano kwa zaka twente chakuti, ndipo ine ndapeza kuti izo zimangochititsa apo chisokonezo. Ngati inu muli nao umboni, uperekeni iwo zisanayambike, mu kusonkhana kwa anthu, pamene Mzimu uli nkudalitsa, ndi zina zotero.

54 Kapena, njira yeniyeni yochitira umboni, si ili mu tchalitchi, ndi kunja mu malo amdima. Lolani nyali yanu iziwala kumene kuli mdima. Muzipita ku manyumba a mmisewu ndi malo osiyana siyana, ndi kumene tchimo ndi chinthu chiri kuwunjikana, ndiye kaloleni Nyali yanu izikawala. Kumeneko ndiko kumalo kokachitira zimenezo.

55 Koma, mulimonsebe, ngati Ambuye akukudalitsani inu ndi kukupatsani inu mdalitso wopambana wapadera, kapena chinachake chimene inu muli nacho choti muwauze anthu, zichitani icho mu nthawi ya utumiki wina uja, utumiki woyambirira, wotsogolera, kapena pamene Mzimu uli nkudalitsa ndi kupereka maumboni ndi mavumbulutso, ndi malirime ndi kutanthauzira, ndi zina zotero, mu kupembedza, kwa oyera, asanati Mawu a Mulungu abweretsedwepo.

56 Ndiye m'busa, akatha kutsogolera nyimbo iyi, nthawi yomweyo atsogolere mpingo mu pemphero, ndi pemphero la osonkhana, iyemwini, pamene iye waima pa nsanja, kuwapempha ena onse kuti aweramitse mitu yawo mu pemphero.

57 Ichi ife tachipeza kuti chiri dalitso lalikulu, ndi chadongosolo kwambiri mu kuchita kwa mu mpingo.

58 Ndiyeno, chinthu chotsatira abusa ayenera azichita ndiye, atatha. Ngati iwo anali ndi msonkhano weniweni wauzimu, ndi mphatso ziri nkuwonetseredwa zinsinsi zambiri za mitima ya anthu, ndi zinthu zimene ziyenera kumachitidwa ndi mphatso mu msonkhano; ndiye Mzimu wa Mulungu uli mu msonkhanowo, ndipo ziri zophweka kwambiri ndiye kuti m'busa awupeze

Mzimu wa Mulungu (umene uli kale mu msonkhanowo) pa Mawu a Mulungu, pamene iye akuwerenga ndi kuyamba kulalikira. M'busa ndiye azilalikira chirichonse chimene Mzimu Woyera ungaike pa mtima wake, chirichonse chimene iye akufuna kuti achite, ataima pamenepo.

59 Koma osonkhana ali oti basi . . . Iwo akhoza kumasangalala, pamene iye akulalikira, ndithudi, kapena kunena "ameni" pamene Mawu akubwera apo. Koma, kufikira pa kuimirira ndi kupereka mauthenga mu malirime ndi kutanthauzira, pamene Mzimu Woyera ukugwira ntchito kudzera mwa m'busayo, Lemba limatsutsa zimenezo, ndipo linati, "Mzimu wa mneneri umamumvera mneneri."

60 M'busa ndiye ayenera kuti azimuuza munthu uyu akhale pansi, ndi kuwapempha iwo kuti akhale molemekeza ndi kusunga malo awo. M'busa azikhala mwamuna amene ali ndi njira yodzichepetsa kwambiri pa iye, koma osati wodzichepetsa kwambiri koma chomwe iye angakhale ngati Ambuye Yesu Khristu pamene Iye anawona cholakwika chikuchitika mu mpingo, Iye anapota zingwe ndipo anawathamangitsa iwo nawatulutsa mu tchalitchi. Ndipo tsopano Mpingo wa Mulungu uli nyumba ya chiweruzo, ndipo m'busa ndiye dongosolo lapamwamba kwambiri mu Mpingo. Mkulu ali chinthu chapamwamba kwambiri mu Mpingo wautumwi, kunja kwa Mzimu Woyera. Mzimu Woyera umabweretsa Uthenga Wake molunjika kwa mkuluyo, ndipo mkuluyo amawupereka Iwo kwa anthu.

61 Oyera ndi mphatso zawo azikhala ndi malo awo, poyamba, kuti azipembedza ndi kubwera palimodzi, zomwe zimabweretsa (monga ine ndanena kale) Mzimu wa Ambuye, mu nyumbayo, kwa abusa. Ndipo izo zimapangitsa izo kukhala zophwekerapo kwa Mzimu Woyera kuti ugwire ntchito kudzera mwa iye ndiye, pamene msonkhano waukulu wauzimu wangotsogolera kuphunzitsa kwake; ndiyeno Mzimu Woyera umalowa mu Mawu ndi kuwaphunzitsa Mawu; utangowonetseredwa kumene mwa mphatso.

62 Ndiyeno kuitanira pa guwa kuli kuchitidwa pamenepo, pambuyo pake, ndipo ambiri ndiye awona ndi kudziwa, molingana ndi kugwira ntchito kwa Mzimu Woyera, ndi Mawu a Mulungu amene m'busa akuwayika Iwo apo, kuti inu ndinu Mpingo wa Mulungu wamoyo. Ndipo monga Paulo ananena, kalelo, "Iye angagwere pansi ndi kunena, 'Zoonadi, Mulungu ali nanu.'"

Tsopano, mu zinthu izi, mulole izo kuti zizichitidwa ndi kulemekeza.

63 Ndipo tsopano kwa abusa, kwa M'bale Neville, pa nthawi iyi. Kumbukirani, iye ndiye mutu wamphumphu wa mpingowu. M'bale Neville ali ndi ufulu wochita ulamuliro wina uliwonse

umene Mzimu Woyera ungafune, chirichonse chomwe Mzimu Woyera ungamupangitse iye kuti anene, mwa kunena kwina. Mu mpingo, ali ndi ufulu pa chirichonse chomwe Mulungu angamutsogolere iye kuti achite. Iye aponso ali nao ufulu pa gulu lake la madikoni. Iye akhoza kulisintha gulu la madikonilo, asungichuma, k—kapena oyimba piyano, kapena udindo wina uliwonse mu mpingo womwe iye akukhumba kuti awusinthe, akamverera kutsogozedwa mwa Mzimu Woyera kuti achite choncho. Ndipo chirichonse chimene iye achita, ine ndizichivomereza icho, pamene iye (ine ndikukhulupirira) kuti ndi munthu waumulungu. Ine ndizizivomereza izo kuti ndi za Ambuye, ine ndizigwirizana nazo chimodzimodzi, kotero izo zikumupatsa iye ulamuliro ndiye kuti aziwuyendetsa mpingo momwe iye akumverera kutsogoleredwa kuti azichitira. Tsopano, kapena, udindo wina uliwonse mu mpingo, ngati iye akufuna k—k—kuti asinthe udindo wa anthu, iye ali ndi ulamuliro woti azichita zimenezo. Zomwe, ine ndikudalira kuti izi nthawizonse zizikhala ziri zokondeka ndipo sizisowa kuti zizigwiritsidwa ntchito.

64 Tsopano Ambuye atakudalitsani inu nonse. Ndipo ine ndikudalira kuti izi zikhala zikuchitidwa mwa kupambana kumene kwa kudziwa kwanu. Ndipo Mzimu Woyera atamakuyang'anirani pa aliyense wa inu.

65 Ndipo waudindo aliyense wa mpingowu atenge malo ake aliwonse a ntchitoyo, akudziwa izi, kuti Mulungu adzakutengani inu woyankhira chifukwa cha momwe inu munatengera udindo wanu mu mpingo. Aliyense adzayenera kudzapereka chofotokoza.

66 Ndipo kwa ena onse, ndi oyera okondedwa amphatso amene ali mu mpingo wathu, iwo a—amene amalosera, kapena amayankhula mu malirime, kapena kutanthauzira, kapena kukhala ndi mavumbulutso, ife tiri okondwa basi kukhala nanu inu mu utumikiwu. Ndipo ife tizikupatsani inu chigwirizano champhumphu mu chirichonse chimene Mzimu Woyera uti udzatsimikizire kuti Iye wanena kwa inu. Ndipo ife tikukukondani inu. Ndipo ife tikukhulupirira kuti mphatso izi ziri mwa inu, ndipo, ngati inu muli nao mwayi woyenera, ndi kafotokozedwe ka Mwamalemba ka izo, kuti inu mukhala ogwira ntchito opambana pakati pathu. Ndipo Ambuye atakudalitsani inu nonse, ndilo pemphero langa lodzipereka.

67 Akhristu, chiyambireni kumvetsera ku tepi iyi, ine ndiri ndi chinthu chimodzi chimene ine ndawona kuti ine ndinachisiya, ndipo chimenecho ndi ichi: kuti, pamene anthu akuyankhula ndi malirime, izo zizikhala mwa kutsatirana kwa "awiri kapena atatu," molingana ndi Lemba. Ndiko kuti, pazikhala mauthenga awiri kapena atatu okha amene aziperekedwa mu utumiki umodzi uliwonse. Zikatha izo molingana ndi Malemba, kuti, "Kutsatirana uku kuzingokhala kuli awiri okha, kapena atatu."

Kotero inu muzizichita zinthu izi moyenera, momwe Mzimu Woyera watsogolerera izo mu Baibulo Lake. Ndipo izi ziri, mwa kupambana kwa kudziwa kwanga, momwe mungamachitire izo. Paulo anati, “Muziwalola awo azikhala, awiri kapena atatu, pamene iwo akuyankhula.” Ambuye akudalitseni inu.

Khalidwe Dongosolo ndi Chiphunzitso cha Mpingo, Bukhu Lachiwiri
(Conduct, Order And Doctrine Of The Church, Volume Two)

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham olalikidwa ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Ndipo kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org